# Maphunziro a m’Baibulo

Bible studies

## Kulengedwa kwa zonse ndi kucimwa koyamba

1. Kulengedwa kwa kumwamba ndi dziko lapansi
2. Kulengedwa kwa munthu
3. Pokhala pace pa munthu
4. Kucimwa kwa Adamu ndi Hava (1)
5. Kucimwa kwa Adamu ndi Hava (2)

## 1. Kulengedwa kwa kumwamba ndi dziko lapansi

**Genesis 1.1-19**

1Paciyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi.
2Dziko lapansi ndipo linali lopanda kanthu; ndipo mdima unali pamwamba pa nyanja; ndipo mzimu wa Mulungu unaliokufungatira pamwamba pa madzi.
3Ndipo anati Mulungu, Kuyere; ndipo kunayera.
4Ndipo anaona Mulungu kuti kuyerako kunali kwabino: ndipo Mulungu analekanitsa kuyera ndi mdima.
5Ndipo Mulungu anacha kuyerako Usana, ndi mdimawo anaucha Usiku. Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku loyamba.
6Ndipo anati Mulungu, Pakhale thambo pakati pa madzi, lilekanitse madzi ndi madzi.
7Ndipo Mulungu anapanga thambo, nalekanitsa madzi anali pansi pa thambolo ndi madzi analf pamwamba pa thambolo: ndipo kunatero.
8Ndipo Mulungu analicha thambolo Kumwamba. Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku laciwiri.
9Ndipo anati Mulungu, Madzi a pansi pa kumwamba asonkhane pamodzi pa malo amodzi, uoneke mtunda: ndipo kunatero.
10Ndipo Mulungu adaucha mtundawo Dziko lapansi; kusonkhana kwa madziko ndipo adaucha Nyanja: ndipo anaona Mulungu kuti kunali kwabwino.
11Mulungu ndipo anati, Dziko lapansi limere maudzu, therere lobala mbeu, ndi mtengo wazipatso wakubala zipatso monga mwa mtundu wace, momwemo muli mbeu yace, pa dziko lapansi:
ndipo kunatero.
12Ndipo dziko lapansi linamera maudzu, therere lobala mbeu monga mwa mtundu wace, ndi mtengo wakubala zipatso, momwemo muli mbeu yace, monga mwa mtundu wace; ndipo anaona Mulungu kuti kunali kwabwino.
13Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku lacitatu.
14Ndipo Mulungu anati, Pakhale zounikira pa thambo la kumwamba, zakulekanitsa usana ndi usiku; zikhale zizindikiro ndi nyengo, ndi masiku, ndi zaka;
15zikhale zounikira m'thambo la kumwamba, kuti ziunikire pa dziko lapansi; ndipo kunatero.
16Ndipo Mulungu anapanga zounikira zazikuru ziwiri; counikira cacikuru cakulamulira usana, counikira cacing'ono cakulamulira usiku, ndi nyenyezi zomwe.
17Mulungu ndipo adaika zimenezo m'thambo la kumwamba, kuti ziunikire pa dziko lapansi,
18nizilamulire usana ndi usiku, nizilekanitse kuyera ndi mdima: ndipo anaona Mulungu kuti kunali kwabino.
19Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku lacinai.

**Mafunso**

1. Kodi ndi yani amene nalenga kumwamba ndi dziko lapansi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Mulungu analenga ciani pa tsiku laciwiri? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Mulungu analenga ciani pa tsiku lacitatu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Mulungu analenga ciani pa tsiku lacinai? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Mulungu anaganiza ciani ku zilengedwe zace? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi tingaphunzire ciani m'nkhani iyi?

## 2. Kulengedwa kwa munthu

**Genesis 1.20-31**

20Ndipo anati Mulungu, Madzi abale zocuruka zamoyo zoyendayenda, ndi mbalame ziuluke pamwamba pa dziko lapansi ndi pamlengalenga.

21Mulungu ndipo adalenga zinsomba zazikuru ndi zoyendayenda zamoyo zakucuruka m'madzi mwa mitundu yao, ndi mbalame zamapiko, yonse monga mwa mtundu wace: ndipo anaona Mulungu kuti kunali kwabwino.

22Mulungu ndipo anadalitsa zimenezo, nati, Zibalane, zicuruke, zidzaze madzi a m'nyanja, ndi mbalame zicuruke pa dziko lapansi.

23Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku lacisanu.

24Ndipo adati Mulungu, Dziko lapansi libale zamoyo monga mwa mitundu yao, ng'ombe, ndi zokwawa, ndi zinyama za dziko lapansi monga mwa mitundu yao: ndipo kunatero.

25Ndipo Mulungu anapanga zinyama za dziko lapansi monga mwa mitundu yao; ndi ng'ombe monga mwa mtundu wace, ndi zonse zakukwawa pansi monga mwa mitundu yao; ndipo Mulungu anaona kuti kunali kwabwino.

26Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'cifanizo cathu, monga mwa cikhalidwe cathu: alamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa ng'ombe, ndi pa dziko lonse lapansi, ndi pa zokwawa zonse zakukwawa pa dziko lapansi.

27Mulungu ndipo adalenga munthu m'cifanizo cace, m'cifanizo ca Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo
mwamuna ndi mkazi. 28Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, Mubalane, mucuruke, mudzaze dziko lapansi, muligonjetse: mulamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakukwawa pa dziko lapansi.

29Ndipo anati Mulungu, Taonani, ndakupatsani inu therere lonse lakubala mbeu liri pa dziko lapansi, ndi mitengo yonse m'mene muli cipatso ca mtengo wakubala mbeu; cidzakhala cakudya ca inu:

30ndiponso ndapatsa zinyama zonse za dziko lapansi, ndi mbalame zonse za m'mlengalenga, ndi zakukwawa zonse za dziko lapansi m'mene muli moyo, therere laliwisi lonse likhale cakudya: ndipo kunatero.

31Ndipo anaziona Mulungu zonse zimene adazipanga, ndipo, taonani, zinali zabwino ndithu. Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku lacisanu ndi cimodzi.

**Mafunso**

1. Kodi Mulungu analenga ciani pa tsiku lacisanu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Mulungu anacita ciani pa tsiku lacisanu ndi cimodzi kulingana ndi ndime ya 26?
3. Mulungu anapatsa munthu kulamulira pa zonse zimene zidalengedwa. Tiyeneranso kusamalira zolengedwa mocenjera. Kodi tingacite bwanji ici? Kodi tingaononga bwanji zolengedwa?
4. Mulungu sanalengedwe anthu cabe komanso anawasamalira: anawapatsa cakudya. Kodi anawapatsa cakudya cotani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Mulungu amasamalirabe zolengedwa zake?

**Sewero**

| | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|
| K | U | M | W | A | M | B | A |
| U | K | A | A | M | B | W | U |
| L | I | Y | E | W | A | I | A |
| E | S | N | A | N | A | N | I |
| N | T | H | A | M | B | O | E |
| G | N | S | G | A | Z | O | N |
| A | U | M | I | Z | M | S | E |

⇨ ……………………………………………………………………………………

| | |
|---|---|
| Kulenga | Kumwamba |
| Thambo | Tsiku |
| Mzimu | Usana |
| Bwino | Mawa |

## 3. Pokhala pace pa munthu

**Genesis 2.15-25**

15Ndipo Yehova Mulungu anatenga munthuyo, namuika iye m'munda wa Edeni kuti aulime nauyang'anire.
16Ndipo Yehova Mulungu anamuuza munthuyo, nati, Mitengo yonse ya m'munda udyeko;
17koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa, usadye umenewo; cifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo
udzafa ndithu.
18Yehova Mulungu ndipo anati, Si kwabwino kuti munthuakhale yekha; ndidzampangira womthangatira iye.
19Ndipo Yehova Mulungu anaumba ndi nthaka zamoyo zonse za m'thengo, ndi mbalame zonse za
m'mlengalenga; ndipo anapita nazo kwa Adamu kuti aone maina omwe adzazicha; ndipo maina omwe onse
anazicha Adamu zamoyo zonse, omwewo ndiwo maina ao.
20Adamu ndipo anazicha maina zinyama zonse, ndi mbalame za m'mlengalenga ndi zamoyo zonse za
m'thengo: koma kwa Adamu sanapezedwa womthangatira iye.
21Koma Yehova Mulungu anamgonetsa Adamu tulo tatikuru, ndipo anagona: ndipo anatengako nthiti yace
imodzi, natsekapo ndi mnofu pamalo pace:
22ndipo nthitiyo anaicotsa Yehova Mulungu mwa Adamu anaipanga mkazi, ndipo ananka naye kwa Adamu.
23Ndipo anati Adamu, Uyu tsopano ndiye pfupa la mafupa anga, ndi mnofu wa mnofu wanga; ndipo
adzachedwa Mkazi, cifukwa anamtenga mwa mwamuna.
24Cifukwa cotero mwamuna adzasiya atate wace ndi amace nadzadziphatika kwa mkazi wace: ndipo
adzakhala thupi limodzi.
25Onse awiri ndipo anali amarisece, mwamuna ndi mkazi wace, ndipo analibe manyazi.

**Mafunso**

1. Kodi munthu anayenera kucita ciani m’munda wa Edeni? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi cinali cololeka kudya zipatso za mitengo iliyonse? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Mulungu analenga bwanji mkazi wa Adamu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Mulungu anamupatsa Adamu mkazi wace. Kodi mukafunafuna mkazi kapena mwamuna, mudzapemphera Mulungu kuti mupeze munthu wabwino ndi woopa Mulungu?
5. Mulungu ndi Mwini wa zimene anazilenga. Anakulenganso. Kodi mumalemekeza ndi kumvera Mwini wako? Ngati inde, mumacita bwanji ici? Ngati iai, ndi cifukwa ciani mukana kulemekeza Mulungu?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao ndipo pezani yankho

| 11 | 15 | 13 | 1 |
|---|---|---|---|
| | | | |

| 11 | 21 | 25 | 1 | 13 | 2 | 9 | 18 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | |

| 16 | 1 |
|---|---|
| | |

| 3 | 8 | 9 | 25 | 1 | 13 | 2 | 9 | | 3 | 8 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | |

| 13 | 1 | 12 | 5 | 14 | 7 | 5 | 4 | 23 | 5 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | |

| 1 | 14 | 1 | 23 | 1 | 16 | 1 | 14 | 7 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | |

| 13 | 23 | 1 | 13 | 21 | 14 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |

| 14 | 4 | 9 |
|---|---|---|
| | | |

| 13 | 11 | 1 | 26 | 9 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A 1 | B 2 | C 3 | D 4 | E 5 | F 6 | G 7 | H 8 | I 9 | J 10 | K 11 | L 12 | M 13 |
| N 14 | O 15 | P 16 | Q 17 | R 18 | S 19 | T 20 | U 21 | V 22 | W 23 | X 24 | Y 25 | Z 26 |

# 4. Kucimwa kwa Adamu ndi Hava (1)

**Genesis 3.1-8**

1Ndipo njoka inali yakucenjera yoposa zamoyo zonse za m'thengo zimene anazipanga Yehova Mulungu,
Ndipo inati kwa mkaziyo, Ea! kodi anatitu Mulungu, Usadye mitengo yonse ya m'mundamu?
2Mkaziyo ndipo anati kwa njoka, Zipatso za mitengo ya m'mundamu tidye.
3Koma zipatso za mtengo umene uti m'kati mwa munda, Mulungu anati, Musadye umenewo, musakhudze
umenewo, mungadzafe.
4Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, Kufa simudzafai;
5cifukwa adziwa Mulungu kuti tsiku limene mukadya umenewo, adzatseguka maso anu, ndipo mudzakhala
ngati Mulungu, wakudziwa zabwino ndi zoipa.
6Ndipo pamene anaona mkaziyo kuti mtengo unali wabwino kudya, ndi kuti unali wokoma m'maso, mtengo
wolakalakika wakupatsa nzeru, anatenga zipatso zace, nadya, napatsanso mwamuna wace amene ali nave,
nadya iyenso,
7Ndipo anatseguka maso ao a onse awiri, nadziwa kuti anali amarisece: ndipo adasoka masamba amkuyu,
nadzipangira mateweta.
8Ndipo anamva mau a Yehova Mulungu alinkuyendayenda m'munda nthawi yamadzulo: ndipo anabisala
Adamu ndi mkazi wace pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda.

**Mafunso**

1. Kodi njoka inati ciani kwa mkazi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi mkazi anayanka ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi njoka inati ciani kugonjetsa mkazi kuti adye cipatso ca mtengo kulingana ndi ndime ya 4 ndi 5?
4. Kodi cotsatira ca kudya cipatso cinali cotani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu. Kocikera nthawi iyi anthu onse samamvera Mulungu. Patsa zitsanso ziwiri zakuti tingakhale bwanji osamvera Mulungu m'masiku onse.
6. Kodi Adamu ndi Hava anacita ciani atamva mau a Yehova? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Cifukwa ca cimo yao Adamu ndi Hava sanakhalebe osangalala monga ankakhala kale. Kodi macimo athu angacotsedwe bwanji kuti tikhale osangalala m'coonadi?

## Sewero

Lembani malembo pa malo ao

**Masalimo 32.1**

| 24 | 15 | 4 | 1 | 12 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 13 | 21 | 14 | 20 | 8 | 21 | 25 | 15 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | |

| 23 | 15 | 11 | 8 | 21 | 12 | 21 | 12 | 21 | 11 | 9 | 4 | 23 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | | |

| 20 | 3 | 8 | 9 | 13 | 15 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 12 | 1 | 11 | 5 |
|---|---|---|---|
| | | | |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A 1 | B 2 | C 3 | D 4 | E 5 | F 6 | G 7 | H 8 | I 9 | J 10 | K 11 | L 12 | M 13 |
| N 14 | O 15 | P 16 | Q 17 | R 18 | S 19 | T 20 | U 21 | V 22 | W 23 | X 24 | Y 25 | Z 26 |

## 5. Kucimwa kwa Adamu ndi Hava (2)

**Genesis 3.9-24**


9Ndipo Yehova Mulungu anaitana mwamunayo nati kwa iye, Uli kuti?
10Ndipo anati, Ndinamva mau anu m'mundamu, ndipo ndinaopa cifukwa ndinali wamarisece ine; ndipo ndinabisala.
11Ndipo anati, Ndani anakuuza iwe kuti uli wamarisece? Kodi wadya za mtengo uja, umene ndinakuuza iwe kuti usadye?
12Ndipo anati mwamunayo, Mkazi amene munandipatsa ine kuti akhale ndi ine, ameneyo anandipatsa ine za mtengo, ndipo ndinadya.
13Ndipo Yehova Mulungu anati kwa mkaziyo, Ciani cimene wacitaci? Ndipo anati mkaziyo, Njoka inandinyenga ine, ndipo ndinadya.
14Ndipo anati Yehova Mulungu kwa njokayo, Cifukwa kuti wacita ici, wotembereredwa ndiwe wopambana ndi zinyama zonse ndi zamoyo zonse za m'thengo: uziyenda ndi pamimba pako, uzidya pfumbi masiku onse a moyo wako:
15ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace.
16Kwa mkaziyo ndipo anati, Ndidzacurukitsa kusauka kwako ndi potenga mimba pako; udzasauka pakubala: udzakhumba mwamuna wako, ndipo iye adzakulamulira iwe.
17Kwa Adamu ndipo anati, Cifukwa kuti wamvera mau a mkazi wako, nudya za mtengo umene ndinakuuza iwe kuti, Usadyeko; nthaka ikhale yotembereredwa cifukwa ca iwe; m'kusauka udzadyako masiku onse a moyo wako:
18minga ndi mitula idzakubalira iwe; ndipo udzadya therere la m'thengo:
19m'thukuta la nkhope yako udzadya cakudya, kufikira kuti udzabwerera kunthaka: cifukwa kuti m'menemo unatengedwa: cifukwa kuti ndiwe pfumbi, ndi kupfumbiko udzabwerera.
20Ndipo mwamuna anamucha dzina la mkazi wace, Hava; cifukwa ndiye amace wa amoyo onse.
21Yehova Mulungu ndipo anapangira Adamu ndi mkazi wace maraya azikopa, nawabveka iwo.
22Ndipo anati Yehova Mulungu, Taonani, munthuyo akhala ngati mmodzi wa ife, wakudziwa zabwino ndi zoipa: ndipo tsopano kuti asatambasule dzanja lace ndi kutenga za mtengo wa moyo, ndi kudya, ndi kukhala ndi moyo nthawi zonse,
23Yehova Mulungu anamturutsa iye m'munda wa Edene, kuti alime nthaka m'mene anamtenga iye.
24Ndipo anamuingitsa munthuyo; nakhazika Makerubi ca kum'mawa kwace kwa munda wa Edene, ndi lupanga lamoto lakuzungulira ponsepo, lakusunga njira ya ku mtengo wa moyo.

**Mafunso**

1. Kodi Adamu anayankha ciani pamene Mulungu anamufunsa kumene analiri? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Adamu anayankha ciani pamene Mulungu anamufunsa ngati anadya cipatso ca mtengo? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Hava anayankha ciani pamene Mulungu anamfunsa ngati anadya cipatso ca mtengo? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi mumacita ciani pamene ena akamba kuti mwacita coipa?
5. Werenganinso ndime ya 15. Ndi m’ndime iyi tawerenga kuti Wina azagonjetsa Satana. Kodi ndani ndi wamphamvu kuposa Satana?
6. Kodi Adamu ndi Hava analoledwa kukhalabe m’munda wa Edeni?
7. Cifukwa ca cimo zonse zinakhala zobvuta: anthu ayenera kusewenza kwambiri, nyama zidzafa, anthu akhala odwala ndipo amwalira. Ngati macimo anu akhululukidwa mungakhale osangalala. Kodi ndi yani amene akwaniritsa kukhululukira macimo anu?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao




→ ........................................................................................ 1 Yohane 2.1

| | | |
|---|---|---|
| Yehova | Edeni | usadye |
| Mulungu | munda | Adamu |
| moyo | nati | iwe |
| nkhope | mtengo | njoka |
| Satana | mkazi | mbeu |
| mau | udani | therere |
| lupanga | mutu | |